# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA LILONGWE M'DZINJA LA 2024-2025

# DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezereka kukhuzidwa ndi La Nina wocheperako mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific.


Boma la Lilongwe likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika.

## October 2024





Mwezi wa October ukuyembekezereka kukhala wopanda mvula koma mvula yochepa ikuyembekezereka kugwa m'madera ena. Mvula ya chizimalupsya itha kugwa m'madera ochepa, yosaposera mlingo wa 20mm.
Mphepo yamkuntho ndi kamvuluvulu zikuyembekezereka mu October.

## November 2024





Mvula ya mulingo wa 20-150mm ikuyembekezereka kugwa m'boma la Lilongwe. Madera ambiri m'bomali akhoza kulandira mvula yocheperako mulingo okhadzikika. Komabe madera ozungulira T/A Mazengera atha kulandira mvula ya mulingo wa 130-150mm

## December 2024





Mvula yochuluka kufika mulingo wa 100-180mm ikuyembekezeredwa m'madera ambiri. Madera a kumadzulo kwa T/A Chadza atha kulandira Mvula yocheperako mulingo okhadzikika.
Madera ena ochepa monga kwa TA Chiseka, Khongoni ndi Chitukula atha kulandira mvula ya mulingo okhadzikika kapena kuposerapo
Mvula yodzalira ikuyembekezereka kugwa m'sabata yachiwiri ndi yachitatu ya December. Koma madera ena atha kulandira mvula yodzalira mofulumirako.

## January 2025





Mvula yamlingo wokhazikika ndikuposerapo ikuyembekezereka m'madera ambiri koma mvula yochuluka ikuyembekezereka kugwa madera a kuzambwe kwa TA Mazengera ndi ku mpoto kwa SC Mtema mulingo oposera 300mm. Madera ena monga a TA Kalolo, Chanza ndi Kumvuma kwa T/A Mazengera atha kulandira mvula yocheperako.

## February 2025




Mvula yochuluka ya mulingo okwana 250mm ikuyembekezereka kugwa madera ena monga SC Mtema ndi ku mpoto kwa TA Chiseka. Koma madera ambiri a m'bomali akuyembekezereka kulandira mvula ya mulingo wa pakati pa 150-200mm


## March 2025




Madera ambiri mu Lilongwe adzalandira mvula yochepa ya mlingo wosaposa 150mm. Madera ochepa aku madzulo kwa TA Kalolo ndi Mazengera atha kulandira mvula ya mulingo okwana 250mm.

Nyengo ya dzinja ku Lilongwe ifika kumathero kuyambira sabata yachiwiri mpaka sabata yachitatu ya March 2025.


## April 2025




Madera ambiri akuyembekereka kulandira mvula yosaposa mulingo wa 50mm.
Komabe madera ochepa ozungulira TA Mazengera ndi Chitseka adzalandira mvula ya pakati pa 100-130mm.

Boma la Lilongwe likuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wokhazikika. Mvula yobzalira iyembekezeredwe mu sabata yachiwiri mpaka yachitatu ya December 2024 Koma madera ena atha kulandira mvula yodzalira mofulumirako pamene mathero a mvula atha kukhala sabata yachiwiri mpaka sabata yachitatu ya March 2025.Dzinja lonse likhala lotalika pakati pa masiku 100-140. Pali chiopsezo cha ng'amba yosaposera sabata imodzi mu January ndi February 2025.

| CHITEDZE | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1 | 13 | 12 |
| NOV | 44 | 102 | 23 |
| DEC | 141 | 200 | 154 |
| JAN | 194 | 271 | 243 |
| FEB | 171 | 216 | 178 |
| MAR | 85 | 189 | 179 |
| APR | 13 | 44 | 45 |





**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: